

Malonje kuchokera kwa Bhatupe Mhango



Genève décembre 2008 © Isabelle Meister

Ine ndine ndani?

---

Ndinabadwira ku Lilongwe, Malawi ndipo ndiri ndi zaka 30 zakubadwa. Monga mayi anga anali wogwira ntchito ya ukazembe, ndakulira ku Malawi, Mozambique ndi ku Zambia. Pamene ndinali ku college ku Malawi, nditayezetsa ndinapezeka kuti ndinali ndi kachiroombo ka HIV ndipo ndakhala ndi kachiroombo kameneka kwa zaka zokwanira zisanu ndi zitatu. Itadutsa nthawi yodzidzimuka ndi nkhani imeneyi, chikhulupiriro chachikhristu changa, ndi chikhumbokhumbo chofuna kukhala ndi moyo ndi nayamba mankhwala a ma ARV zinathandizira kutsekula moyo wina watsopano mmoyo wanga. Ndinalumikizina ndi gulu la anthu ogwira ntchito ndipo posakhalitsa ndinakhala liwu la anthu amene ali ndi kachiroombo ka HIV. Ndakhala ndi kugwira ntchito ngati Co-ordinator wa bungwe lotchedwa UN Plus Global limene liri pansu pa UNAIDS ndisanapitenso kukapitiriza maphunziro mu mwezi wa August 2010 a ukachenjede a MBA.

Nkhaniyi ndayi fotohoza  
Chifukwa chani?

---

Ndikugawanana nanu nkhani yanga chifukwa sindikufuna msungwana wina kuti adzapezekenso monga ine ndinaliri pamene akhoza kukhala ndi mwayi wosankha, ndipo kukhala wofooka pamene akadakhala wolimba. Sindikufuna wina aliyense, mwamuna kapena mkazi, kukhala wosadzikonda mosiyana. Kachiroombo ka HIV ndi kakang'ono koma kamafuna chidwi chathu chonse – tonse timafuna zinthu zabwino mmoyo monga kumwa ndi kutha kumva fungo la coffee wabwino! Yakwana nthawi kwa tonse kuti tisiye kupanga anthu openderezedwa kwa anthu amene ali ndi HIV. Yakwana nthawi yakuti aliyense akuyenera kutengapo gawo kupewa HIV, kupereka chithandizo chamankhwala, kusamalira ndi kuthandiza – ndiri ndi chiyembekezo kuti mukhudzidwa ndi nkhanayi ndipo muchitapo kanthu.